EXAMINATIONS No:___________________________

# ZOMBA URBAN DISTRICT MOCK

## 2023 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE EXAMINATION

# CHICHEWA

## (100 MARKS)

LACHINAYI 23 /MARCH/2023

**Subject Number:P032**
**Nathwi :1:00 – 3:15 pm 2 ½ Hrs**

Dzina lanu____________________________________________________________________
**(yambani ndi la bambo)**
Dzina la sukulu yanu:_____________________________________________________________

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6- 10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

**MALANGIZO**

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi limodzi.
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi **A,B,C** ndi **D**.
3. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu yanu** pamwamba pa tsamba lililonse.
4. Lembani **nambala ya mayeso** pamwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani **chimangirizo** kapena **kalata** mu Gawo **A** ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo **B,C** ndi **D**.
6. Yankhani mafunso a mugawo **B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lilonse..
7. Yankhani mafunso amu gawo **D** pozunguliza limbo lokhoza pafunso lililonse..
8. Perekani pepala lanu kwa woyang'anira mayeso pamene mwauzidwa kuti mutero.
9. Mu tebulo lomwe mwapatsidwali, chongani mafunso omwe mwayankha kupatula mafunso 6 mpaka 45.

**Turn Over**

**GAWO A (30 MALIKISI)**
Yankhani funso limodzi mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu: **CHIKONDWELERO CHA KHRISIMASI CHOSAIWALIKA**

   Mwazina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**
- Tchulani chaka ndi kumalo kumene kudachitika chikondwelero
- Kudali anthu angati

**Ndime yachiwiri**
- Tchulani zinthu zimene mudadya ndi kumwa
- Mudakonda kwambiri ziti
- Chifukwa ninji mudazikonda

**Ndime yachitatu**
- Tchulani mitundu ya magule amene adalipo kapena zotsangalatsa zina

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa nzanu yomufotokozera za malo ochititsa chidwi kudera kwanu.

   Tsatani izi polemba

**Ndime yoyamba**
- Dzina la dera lanu
- Dzina la malowo
- Momwe angayendere kuti afike kumaloko.

**Ndime yachiwiri**
- Zinthu zochititsa chidwi kumaloko
- Kasamalidwe ka malowo kuti apitilire kukhala ochititsa chidwi.

**Ndime yachitatu**
- Phindu lomwe anthu a m'deralo amapeza chifukwa cha malowo

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

___________________________________________

**GAWO B (MALIKISI 20)**

**3. KUMVETSA NKHANI**

Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kenaka yankhani mafunso.

Kalekale kudali mudzi wotchuka kwambiri womwe unkatchedwa dzina loti Kunjakulinji. M'mudzimu munadutsa mtsinje waukulu wotchedwa Cheweta. Mtsinjewu udali 'mpulumutsi' kwa anthu a mmudzimu. Anthu ammudzimu ankabzala mbewu zamasamba monga phwetekere, anyezi ndi zina mothinana ndiponso mochititsa chidwi m'mbali mwa mtsinjewu.

Ulimi wa m'mphepete mwa mtsinjewu udachititsa anthu onse a mmudzimu kukhupuka ndiponso kudziwika ponseponse. Anthu ochokera m'madera osiyanasiyana, kuphatikiza a zungu ankakhamukira kumudziwu kuti akawone momwe eni ake mudzi ankachitira ulimi wothirira.

Alendo ambiri omwe ankafika kumudziku adalephera kulangiza mfumu Kunjakulinji ndi anthu ake za kuopsa kwa kukhala m'phepete mwa mtsinje. Mfumuyi idalimbikitsa anthu ake pa ulimi wothilira, kotero kuti anthu adagwetsa mitengo yonse ya mphepete mwa mtsinjewu.

Chaka chotsatira kudabwera mvula yochuluka moti mtsinje udadzadza ndipo madzi adasefukira. Nthaka komanso mbewu zidakokoloka. Anthunso sadathe kulima mbewu zawo mphepete mwa mtsinjewo. Nyumba zidagwa chifukwa cha madzi osefukira aja. Anthu ena m'mudzimo adasowa pokhala kamba kakusamvera kwawo.

**MAFUNSO.**

A. Kodi mtsinje wa Cheweta udadutsa mudzi uti?

________________________________________(2 Malikisi)

B. N'chifukwa chiyani mtsinjewu umatchedwa 'mpulumutsi?'

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

C. Tchulani mbewu ziwiri zomwe anthu ankabzala mphepete mwa mtsinjewu

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

D. Fotokozani chomwe chidachitika kuti anthu okhala mphepete mwa mtsinjewu akhupuke

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

E. Pezani mawu mnkhaniyi omwe akutanthauza 'kelemera'

________________________________________(2 Malikisi)

F. N'chifukwa chiyani anthu amitundu yosiyanasiyana ankakhamukira ku mudzi umenewu

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

G. Ndi langizo lotani lomwe mfumu Kunjakulinji ndi anthu ake adalandira

________________________________________

________________________________________(2 Marks)

H. Kodi mfumu Kunjakulinji adachita chiyani pofuna kusonyeza kusagwirizana ndi anthu ena ankawalangiza?

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

I. Lembani mavuto awiri omwe anthu am'mudziwu adakumana nawo chifukwa chodula mitengo?

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

J. Perekani muti woyenera wa nkhani mwawerengayi

________________________________________

________________________________________(2 Malikisi)

**GAWO C. (MALIKISI 10)**

4. Werengani kankhanika mosamalitsa ndipo muyankhe mafunso otsatirawa

Ndikukumbutseni pano kuti pamene mutentha tchire, kugwetsa mitengo mwachisawawa komanso kuotcha makala mukudziitanira ntchentche pa chilonda.

**Mafunso**

i. Kodi malangizowa angaperekedwe kwenikweni pa mwambo wanji?

________________________________________

________________________________________(1 maliki)

ii. Lembani udindo wa munthu amene angapereke malangizowa

________________________________________(1 Maliki)

iii. Lembani chinthu chimodzi chomwe chingachitike ngati anthu atasankha kusamvera malangizo

________________________________________

________________________________________( 1 Maliki)

iv. Perekani njira ziwiri momwe mungasamalire pogona.

______________________________________________________________________________
______________________________________________________________________(2 Malikisi)

5. **Kupanga ziganizo**
   Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. Nyentchera:____________________________________________________(1 Maliki)
b. Ndi:__________________________________________________________(1 Maliki)
c. Tula mbeta:_____________________________________________________(1 Maliki)
d. Lera:_________________________________________________________(1 Maliki)
e. Popeza:_______________________________________________________(1 Maliki)

**GAWO D (MALIKISI 40)**
**Zungulizani limbo lokhoza (A,B,C kapena D) M'mafunso otsatirawa**

**Mafunso 6 mpaka 10 sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.**

6. Mphaka wadya ndiwo zonse
   A. Mlowamalo  C. Mneni
   B. Mfotokozi  D. Dzina

7. Iye wakhala pa mpando wokongola
   A. Mperekezi  C. Mneni
   B. Mfotokozi  D. Muonjezi

8. Iye wamenyedwa kolapitsa
   A. Mneni  C. Mfotokozi
   B. Muonjezi  D. Mperekezi

9. Iye ndi mbava
   A. Mlumikizi  C. Mperekezi
   B. Mlowammalo  D. Mneni

10. Makaka auma kuti gwa
    A. Mneni  C. Mfotokozi
    B. Mvekero  D. Mperekezi

**Mafunso 11 – 15: sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa mzere mziganizozi**

11. Amayi aphika thobwa
    A. Dzina lopadera  C. Mwininkhani
    B. Dzina loitanira  D. Pantherankhani

12. Aphunzitsi akuphunzitsa
    A. Mwininkhani  C. Dzina lapadera
    B. Dzina loitanira  D. Pantherankhani

13. Takondwa pita kumsika
    A. Dzina lapadera  C. Dzina loitanira
    B. Pamtherankhani  D. Mwininkhani

14. Zuze, chilombo cha mmudzi, wamenyedwa
    A. Dzina loitanira  C. Mwininkhani
    B. Pamtherankhani  D. Dzina lapadera

15. Pemphero ndi mtsikana wabwino.
    A. Mwininkhani  C. Mtsirizitsi wa mneni
    B. Pamtherankhani  D. Dzina loitanira

**Mafunso 16 mpakana 20: sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.**

16. Kuyankhulira nsonga ya lilime
    A. Kupepetsa  C. Kuvomereza
    B. Kunyada  D. Kuziyamikira

17. Bwenzi la mphasa
    A. Munthu wosoka mphasa
    B. Munthu wokonda mphasa
    C. Munthu wodwaladwala
    D. Munthu wosunga mphasa

18. Utsa mapiri pachigwa
    A. Danitsa  C. Dandaula
    B. Dabwa  D. Delera

19. Tchera kumwezi nkhanga zaona
    A. Pusa  C. Lephera
    B. Lakwa  D. Beredwa

20. Bisala Pachipande
    A. Phimba  C. Zemba
    B. Nama  D. Kana

**Mafunso 21 mpaka 25: sankhani misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizozi.**

21. Anyamata avula zipewa zawo
    A. Wochititsa  C. Wochitirana
    B. Wochita  D. Wonyazitsa

22. Mbuzi yagwidwa ndi fisi
    A. Wochitidwa poyera
    B. Wochititsa
    C. Wochitira
    D. Wochitirana

23. Mfiti yalumwa ndi nsato
    A. Otsusana C. Wonyazitsa
    B. Wochitirana D. Obwerezabwereza
24. Efilida amugulira zovala
    A. Wochitidwa C. Wochitidwa mchibisira
    B. Womchitira D. Wochititsa
25. Ana asukulu ali bakhalibakhali kukonzekera mayeso
    A. Wochitidwa C.Wochititsa
    B. Wochitirana D.Wobwerezabwereza

**Mafunso 26 mpaka 30 sankhani ntchito za alumukizi muziganizo zotsatirazi**

26. Amayi agula mpunga ndi nyama lero
    A. Kulumikiza mayina
    B. Kulumikiza aneni
    C. Kulumikiza afotokozi
    D. Kulumikiza aonjezi
27. Dola anabwera ndipo wapita
    A. Kulumikiza aonjezi C.Kulumikiza maina
    B. Kulumikiza aneni D.Kulumikiza afotokozi
28. Mwana wamzeru ndi waulemu amasangalatsa
    A. Kulumikiza aneni
    B. Kulumikiza alowammalo
    C. Kulumikiza aonjezi
    D. Kulumikiza afotokozi
29. Anawa agwira ntchitoyi mwaluso ndi mwamphamvu
    A. Kulumikiza mayina
    B. Kulumikiza afotokozi
    C. Kulumikiza aonjezi
    D. Kulumikiza alowammalo
30. Iye wabwera ngakhale akudwala
    A. Kulumikiza aneni C.Kulumikiza mayina
    B. Kulumikiza afotokoziD.Kulumikiza aonjezi

**Mafunso 31 mpaka 35: sankhani chachikazi cha mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo:**

31. Akuba atibera mphulu zonse.
    A. Tonde C. Nzambwe
    B. Nkhosa D. Mtheno
32. Ife tinalangizidwa ndi ndoda ziwiri.
    A. Namkungwi C. Wakunjira
    B. Ntchembere D. Phungu
33. Galu wagwira kachipsolopsolo kaja
    A. Kathazi C. Kankhunda
    B. Kamsoti D. Kamkota
34. Apatsidwa mzambwe ziwiri kuti awete
    A. Mkota C. Msoti
    B. Nkhunda D. Thadzi
35. Mfumu yawo ndiyabwino
    A. Mfumukazi C. Mtengwa
    B. Mfumakazi D. Ntchembere

**Mafunso 36 mpaka 40: sankhani magulu amayina omwe atsekedwa mzere.**

36. Wamisala wagula chiguduli
    A. U, - Ma C. Chi, - Zi
    B. Mu, - Mi D. Li, - Ma
37. Amayi agula khasu
    A. Li, - Ma C. Ka, - Ti
    B. I, - Zi D. Mu, - A
38. Kadzino kwamwana kaduka
    A. U, - Ma C. Li, - Ma
    B. Ka, - Ti D. I, - Zi
39. Sibwino kukhala ndi ngongole zochuluka
    A. I, - Zi C. Li, - Ma
    B. Chi, - Zi D. Ka, - Ti
40. Dolika wapiti kumudzi
    A. Li, - Ma C. Ka, - Ti
    B. Ku, - Pa, - Mu D. I, - Zi

**Mafunso 40 mpaka 45: sankhani mitundu ya nthambi zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

41. Mbuzi yomwe mwaphayi ndi yanga
    A. Y a mfotokozi C. Ya dzina
    B. Yoyima payokha D. Ya muonjezi
42. Tiyenera kumapita poti kwada.
    A. Ya dzina C. Ya muonjezi
    B. Ya mfotokozi D. Yoima payokha
43. Kuti abwera lero ndizabodza.
    A. Ya muonjezi C. Ya mfotokozi
    B. Ya dzina D. Yoyima payokha
44. Anyamata musakhumudwe ndi zomwe ndikunenazi
    A. Ya muonjezi C. Yoima payokha
    B. Ya dzina D. Ya mfotokozi
45. Iye amayenda ngati akudwala
    A. Ya muonjezi C. Ya mfotokozi
    B. Ya dzina D. Ya mneni

**MAFUNSO ATHERA APA**